PHUMZIRO LA 45

1. Kodi Mulungu anasunga lonjezo lache kwa Zakaliya ndi Elizabeti loŵapatsa mwana wamamuna?
-Inde.

2. Kodi tchito ya mwana wamamuna wa Zakaliya, Yohane, idzakhala yotani?
-Yohane adzakhala patsogolo pa Ambuye, kwakhozera njira lwowo.

3. Kodi Ambuye amene adzaŵakhonzere njira Yohanewo, anali ndani?
-Anali Yesu, Mulungu Mpulumutsi.

4. Kodi Mpulumutsi amene akubwerayo adzakhala bwanji ngati dzuwa limene likuturuka?
-Mpulumutsi adzabwera kudzapereka kuwala pakutha kwa mdima wa Satana ngati m'mene limaperekera kuwala dzuŵa, mdima ukatha.

5. Kodi pali dzuŵa lingati pa dziko la pansi pano?
-Limodzi.

6. Kodi Mulungu analonjeza zotumiza Mipulumutsi ingati?
-M'modzi.

7. Kodi Zakaliya anadziŵa bwanji kuti Mpulumutsi adzabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana?
-Chifukwa chakuti Zakaliya anaŵerenga mu buku la Mulungu limene analonjeza zotumiza Mpulumutsi.

-Zaka zambiri zapitazo, Mulungu anapereka lonjezo kwa Abulahamu, Isaki ndi Yakobo kuti lye adzatumiza Mpulumutsi kudzera mwa zidzukuru zawo.

-Tsopano, zaka zambiri zitatha, Mulungu anasunga lonjezo lache lotumiza Mpulumutsi kudzera mwa zidzukuru za Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

Tiyeni tiŵerenge Mateyo 1:1-2

1-Makolo a Yesu Kilisitu, anali Davide ndi Aburahamu. Motsatira ndandanda wa mayina a makolo akewo ndi awa:
2-Aburahamu anabereka Isaki, Isaki anabereka Yakobo, Yokobo anabereka Yuda ndi abale ache.

-Kodi Yesu anachokera ku mtundu uti?
-Yesu anachokera ku mtundu wa Aburahamu, Isaki ndi Yakobo.

-Yesu, Mulungu Mpulumutsi, anali chidzukulu cha Aburahamu, Isaki ndi Yakobo ngati m'mene analonjezera Mulungu.

-Kodi Yesu anachokera ku mtundu wanji ndipo mfumu yanji yayikuru ya ku Yuda?
-Anachokera ku mtundu wa mfumu Davide.

-Mulungu amasunga malonjezo ache.

-Mulungu samaphwanya malonjezo ache.

-Dzina lina la Yesu linali Kilisito.

-Kodi dzina lakuti Kilisito likumasulira chiyani?
-Dzina lakuti Kilisito likutanthawuza kuti Iye anatumizidwa ndi Mulungu kuti adzakhale Mneneri Wamkulu kwambiri.

-Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kuti adzakhale Mneneri



Mulungu Mpulumutsi, amene ankabwera kuchokera kumwamba kudzakhala ndi anthu.

-Kodi Yosefe anachita chiyani pamene anadzuka kuchokera ku tulo ndiponso ku maloto ache?

Tiyeni tiŵerenge Mateyo 1:24-25

24-Chomcho Yosefe atadzuka, anachita ngati m'mene anamuwuzira mngero wa Ambuye ndipo anamutenga Mariya kukhala mkazi wache,
25-koma sanakhale naye pa malo amodzi mpaka pamene anabereka mwana wamamuna, ndipo Yosefe anamupatsa mwanayo dzina lakuti Yesu.

-Yosefe anamvera zimene Mulungu anamuwuza iye kudzera mwa mngero.

-Yosefe anamutengera ku nyumba kwache Mariya ngati mkazi wache.

-Koma Yosefe sanakhale pa malo amodzi ndi Mariya mpaka pa nthaŵi imene anabereka mwana wache wamamuna.

-Yesu anabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku chilango cha mfa.

Tiyeni tiŵerenge Mateyo 1:22-23

22-Zonsezi zinachitika pokwanilitsa zimene analankhula Ambuye kudzera mwa Mneneri kuti,
23-“Namwali adzakhala ndi pathupi asanakhale pamodzi ndi mamuna, ndipo adzabereka mwana wamamuna, ndiponso mwanayo adzamupatsa dzina lakuti Emanuwelo, “ kutanthawuza kuti, “Mulungu ali ndi ife.”

-Aneneri analankhula kuti Mpulumutsi adzabada mwa namwali.

-Mulungu anasunga lonjezo lache.

-Yesu adzabadwa mwa namwali.

-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu, Iyeyo adzakhala ndi mayina ambiri.

-Dzina lina la Yesu linali “Emanuwelo.”

-Kodi dzina lakuti “Emanuwelo” likutanthawuza kuti chiyani?
-Dzina lakuti “Emanuwelo” likutanthawuza kuti Yesu akubwera kudzakhala ndi anthu.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu ankatchedwa kuti Emanuwelo?
-Chifukwa chakuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi amene ankabwera kudzakhala ndi anthu.

-Mwana wa Mariya amene anakabadwa anali Yesu,



Wamkulu Kwambiri amene adzafotokoze bwino za mawu akulu kwambiri.

-Dzina lakuti Kilisito likutanthawuzanso kuti Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kuti adzakhale Wamsembe wamkulu kwambiri.

-Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kuti adzakhale Wamsembe wamkulu kwambiri amene adzapereke msembe, msembe yoposa msembe zonse.

-Dzina lakuti Kilisito likutanthawuzanso kuti Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kuti adzakhale Mfumu wamkulu kwambiri.

-Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kudzalamulira komanso ngati chidzukulu cha mfumu Davide.

-Yesu anatumizidwa ndi Mulungu kudzakhala mfumu yayikulu kwambiri amene adzalamulire mpaka kalekale.

-Yesu Kilisito yekha ndi amene anaperekedwa lonjezo ndi Mulungu kuti adzakhala Mpulumutsi.

-Yesu Kilisito yekha ndi amene anaperekedwa lonjezondi Mulungu loŵapulumutsa anthu ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana.

-Mulungu anatumiza mngelo kuti akamuwuze Mariya kuti Iye adzabereka Mpulumutsi.

-Koma Mariya anali atatomeledwa ndi mamuna dzina lache Yosefe.

-Apa panali vuto:

-Maliya anali mnamwali, ndipo anatomeledwa ndi Yosefe, koma anali ndi pathupi.

-Chiyambire Yosefe anali asanakhale pa malo amodzi ndi Mariya ndiponso anali asanakwatirane.

-Kodi Yosefe ankaganiza chiyani chifukwa chakuti Mariya anali ndi khanda?

-Yosefe ankaganiza kuti Mariya anakhala pa malo amodzi ndi mamuna wina.

-Chomcho Yosefe anaganiza zomusiya Mariya.

Tiyeni tiŵerenge Mateyo 1:18-19

18-Kubadwa kwa Yesu Kilisitu kunali kotere: Mnamwali otchedwa Mariya, mayi ache a Yesuyo anatomeledwa ndi Yosefe, koma anali asanakhaleko pa malo amodzi, Mariyayo anapezeka kuti ali ndi pathupi mwa mphamvu ya Mzimu Yoyera.
19-Koma Yosefe anali munthu wabwino mtima mwakuti sanafune kumuyalutsa Mariyayo pa maso pa anthu, ndiye chifukwa chache anaganiza zongothetsa chitomelo chawocho mwamseri ndipo mosayimbana mulandu.

-Kodi Mariya anakhala pa malo amodzi ndi mamuna aliyense?
-Iyayi.

-Kodi Mariya anabereka bwanji mwana?
-Mulungu Mzimu Woyera anapanga zodabwitsa, ndipo Mariya anabereka mwana.

-Mwana amene anali m'mimba mwa Mariya anali Mulungu



Mpulumutsi.
-Mulungu sanafune kuti Yosefe amusiye Mariya.

-Chomcho Mulungu anatumiza mngero kukalankhula ndi Yosefe m'maloto.

Tiyeni tiŵerenge Mateyo 1:20-21

20-Yosefe ali nkati moziganizira zimenezi, mngero wa Mulungu anamuwonekera m'maloto ndipo anati, "Yosefe, mwana wa Davide, Usawope kumutenga Mariya kuti akhale mkazi wako. Pakuti pathupi pakepo ndi pa mphamvu ya Mzimu Woyera.
21-Adzabereka mwana wamamuna, ndipo adzamutcha dzina lake Yesu, pakuti Iyeyo ndi amene adzaŵapulumutse anthu ache ku machimo awo."

-Kodi mngero wa Mulungu analankhula chiyani kwa Yosefe m'maloto ache?
-Mngero wa Mulungu analankhula kuti Mariya anali ndi mwana chifukwa chakuti Mzimu Woyera anachita zodabwitsa.

-Mngero wa Mulungu analankhula kuti mwana wa Mariya anali Mulungu Mpulumutsi.

-Mngero wa Mulungu analankhula kuti Yosefe amutenge Mariya ngati mkazi wache.

-Mngero wa Mulungu analankhulanso kuti Yosefe adzamutche mwana wa Mariya dzina lakuti yesu.

-Yesu anali m'dziko muno kudzaŵapulumutsa anthu.

-Yesu anabwera kudzaŵapulumutsa anthu ku machimo awo.